Mose, anakakhala akumukananso Mlungu.

-Buku la Mulungu, Bayibulo, ndi Nthenga wa Mulungu kwa anthu onse.

-Ngati tikukana kuwumvera uthenga wa Mulungu wa M’buku Lake, Bayibulo, ndiye kuti tukukananso kumumvera Mulungu.

-Ngati tikukana kumumvera Mulungu, Mulungu adzatipatsa chilango champaka kalekale.



## PHUNZIRO LA 32

1. Mulungu atamuwononga Farawo ndi asilikali ake Mnyanja Yifiira ija, kodi Iye amkaŵatsogolera a Isirayeli kupita kuti?
-Ku chipululu.

2. Kodi chipululu ndi chiyani?
-Chipululu ndi ku malo kumene kuli mchenga wambiri.

3. Mulungu akuŵatsogolera a Isirayeli mchipululu muja, kodi a Isirayeli anachita chiyani?
-A Isirayeli amkamunena Mose ndi Aloni.

4.Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli amkamunena Mose ndi Aloni?
-Chifukwa chakuti analibe chakudya.

5. Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli analibe chakudya?
-Chifukwa chakuti mchipululu munalibe chakudya.

6. Kodi Mose anakatha kwafunila a Isirayeli chakudya mchipululu muja?
-Iyayi.

7. Kodi a Isirayeli anakatha kudzifunira okha chakudya mchipululu muja?
-Iyayi.

8. Kodi ndi ndani yekha amene anakatha kuwapatsa a Isirayeli chakudya mchipululu muja?
-Mulungu.

9. Kodi chifukwa chiyani Mulungu amaŵa thandiza anthu ngakhale kuti anthuwo sakumukhulupilira Iye.
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi amene anaŵalenga anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu amaŵakonda anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu amafuna kwapulumutsa anthu onse.
-Chifukwa chakuti Mulungu amafuna kuti anthu onse adzimukhulupilira Iye.

10. Ngati sitikukhulupilira mwa Mulungu, Kodi Iye adzatipulumutsa ife?
-Iyayi.

11. Kodi Mulungu anaŵapatsa  Isirayeli nyama yotani madzulo akewo?
-Madzulo akewo, Mulungu anaŵatumizira zimziri a Isirayeli.

12. Kodi ana a Isirayeli anayitcha dzina lakuti chiyani mikate imene anapereka Mulungu ija?
-Mana.

13. Kodi Mulungu anamuwuza Mose kuti achite chiyani kuti apeze madzi?
-Mulungu anamulamula mose kuti akanthe tanthwe ndi ndodo yake kuti madzi atuluke.

14. Kodi ndi ndani yekha amene amene angathe kutipulumutsa ife ku mphamvu ya uchimo, imfa ndi Satana.
-Mulungu yekha.



gaŵawononge."
25-Chomcho Mose anaŵatsikira anthu ndi kulankhula nawo.

-Mulungu anamuwuza Mose kuti a Isirayeli afa akakhudza phirilo.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anamulora Mose kuti akwere pa phiripo?
-Kodi Mose analinso mwana wa Adamu ndi Hava?
-Inde.

-Kodi Mose anabadwiranso m'machimo?
-Inde.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anamulora Mose kuti akwere pa phiripo?

-Chifukwa chakuti Mose anakhulupilira mwa Mulungu.

-Chifukwa chakuti Mose anapita kwa Mulungu m'njira ya Mulunguyo.

-Chifukwa chakuti Mose anapita kwa Mulungu pogwiritsa ntchito njira imene Mulunguyo anamuwonetsa.

-Mulungu anamusankha Mose kuti akhale otumikira Wake.

-Mulungu anamusankha Mose kuti adzitenga mawuthenga kwa Mulungu kupita nawo kwa a Isirayeli.

-A Isirayeli anakakhala kuti akukana kumumvera

-Mulungu amapereka chilango pa tchimo lina lililonse ndi imfa.

-Mu nthaŵi ya Nowa, Mulungu anapereka chilango cha imfa pa machimo a anthu onse.
-Mu nthaŵi ya Sodomu ndi Gomora, Mulungu anapereka chilango cha imfa pa machimo a anthu onse.
-Mu nthaŵi ya Farawo, Mulungu anapereka chilango cha imfa pa machimo a anthu onse.

-Mulungu amalanga machimo onse ndi imfa.

-Mulungu anatsika pamwamba pa phiri la Sinayi, ndipo anamuyitana Mose pamwamba pa phirilo.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 19:20-25

20-AMBUYE anatsika pamwamba pa phiri la Sinayi, anamuyitana Mose kuti apite pamwamba pa phirilo, ndipo Mose anakwera pamwamba pa phirilo
21-ndipo AMBUYE anamuwuza Mose kuti, “Tsika, ndipo ukaŵachenjeze anthu kuti asakalumphe malire kuti andiyang’anitsitse Ine, angafe anthu ambiri.
22-Ngakhale amsembe, oyandikira kwa AMBUYE, nawonso adzipatulitse , AMBUYE angaŵawononge.
23-Ndipo Mose anati kwa AMBUYE, “Anthu sangathe kukwera mphiri la Sinayi; pakuti Inu mwatichenjeza kale, kuti, “Lemba malire mphirimo , ndikulipatula kuti likhale loyera.”
24-Ndipo AMBUYE anati kwa iye, “Pita, tsika; ndipo ukabwere ndi Aloni. Koma amsembe ndi anthu, asapyole kukwera kupita kwa AMBUYE, an-



15. Kodi Mulungu anaŵapulumutsa a Isirayelilayeli malingana ndi njira imene iwo anasankha?
-Iyayi.

16. Kodi Mulungu anaŵapulumutsa bwanji a Isirayeli?
-Malingana ndi njira imene Mulunguyo anasankha.

17. Kodi Mulungu amaŵapulumutsa bwanji anthu onse?
-Malingana ndi njira imene Mulungu amasankha.

-Kodi Mose ndi a Isirayeli ali kuti tsopano?
-Ali m’chipululu.

-Mulungu anapitiriza kwatsogolera a Isirayeli mchipululu.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 19:1

1-A Isirayeli anafika mchipululu cha Sinayi pa tsiku loyamba la mwezi wachitatu chichokeleni ku dziko la Eguputo.

-Kodi ndi ndani amene anakuganizira ku malo kumene a Isirayeli anakapita?
-Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu ndi amene anakuganizira ku malo kumene anakapita a Isirayeli?
-Chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene ankayidziŵa njira yipitira kumenekoko.

-Ngati m’mene Mulungu anayidziŵira njira yakuti a

Isirayeli adutsire popita kwawo, chimodzimodzinso Mulungu amayidziŵa njira yabwino ya anthu onse yopitira kwa Iye.

-Kodi kenako Mulungu anaŵatsogolera a Isirayeli kupita kuti?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 19:2

2-Atachoka ku Lefidimu anakafika ku chipululu cha Sinayi, ndipo anamanga masakasa awo patsogolo pa phiri la Sinayi.

-Mulungu anaŵatsogolera a Isirayeli kupita ku phiri la Sinayi.

-Kodi mukulikumbukira phiri la Sinayi?
-Pa phiri la Sinayi ndi pamene Mulungu analankhula kwa Mose kupitira mu chithukuluzi chimene chimkayaka koma osapselera chija.

-Kodi Mulungu analonjeza chiyani kwa Mose atalankhula kwa iye kuchokera mu chithukuluzi chimene chimkayaka koma osapselera chija?
-Mulungu analonjeza kuti adzamubweretsanso Mose pa phiri la Sinayi.

-Kodi Mulungu analisunga lonjezo lake lakuti adzamubweretsanso Mose pa phiri la Sinayi?
-Inde.

-Ngakhale kuti Farawo ankafuna kumupha Mose, Mulungu anamutchinjiriza Mose mpaka anamubweretsa pa phiri.



18-Ndipo phiri la Sinayi linafuka utsi, popeza AMBUYE anatsikira m’moto pamenepo. Ndipo utsi wake unakwera ngati utsi wa ng’anjo, ndipo phiri lonse linagwedezeka kwambiri.

-Mulungu anatsika pa phiri la Sinayi.

-Mabingu anagwedeza mlengalenga onse wozungulira phirilo.

-Mphezi inang’anima pa malo ponse pozungulira phirilo.

-Utsi wakuda kwambiri unavundikira pa mwamba ponse pa phirilo.

-Kulira kwakukulu kwa lipenga kunamveka.

-Phiri lonse linagwedezeka kwambiri.

-Ndipo Mulungu anatsika m’moto pamwamba pa phirilo.

-Kodi a Isirayeli anagwidwa ndi mantha?
-Inde, anawopa kwambiri.

-Kodi mabingu, mphezi, utsi wakuda ndi moto ndi zizindikiro za chiyani?

-Ndi zizindikiro zakuti:
-Mulungu ndi oyera.
-Mulungu amadana ndi tchimo lina lililonse.

-Chifukwa chakuti Mulungu samkafuna kuti wina aliyense alikhuze phirilo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sankafuna kuti wina aliyense alikhuze phirilo?
-Chifukwa chakuti Mulungu ankafuna kutsika mphirimo.

-Kodi chinakachitika ndi chiyani a Isirayeli anakalikhudza phirilo?
-Anakafa.

-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli anakafa anakalikhudza phirilo?
-Chifukwa chakuti Mulungu ankatsika pa phiripo.

-Chifukwa chakuti Mulungu ndi oyera.
-Chifukwa chakuti Mulungu amadana ndi tchimo lina lililonse.
-Chifukwa chakuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lina lililonse ndi imfa.

-M'maŵa mwa tsiku lachitatu lakelo, Mulungu anatsika pa phiri la Sinayi.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 19:16-18

16-Kum'maŵa kwa tsiku lachitatu, kunali mabingu ndi mphezi, ndi mtambo wakuda pa phiripo, ndi kulira kwa lipenga kwakukulu. Ndipo anthu onse okhala ku tsasa ananjenjemera.
17-Ndipo Mose anaŵatulutsa anthu ku tsasa, kuti akumane ndi Mulungu; ndipo anayima pa tsinde



etsanso iye pa phiri la Sinayi.

-Tingathe kumakhulupilira malonjezo onse amene Mulungu amapereka chifukwa chakuti Mulungu amasunga malonjezo ake onse.

-Mose ndi a Isirayeli atafika pa phiri la Sinayi, Mulungu anamuyitana Mose kuti apite pamwamba pa phirilo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamuyitana Mose kuti apite pamwamba pa phirilo?
-Chifukwa chakuti Mulungu ankafuna kulankhulana ndi Mose.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 19:3-5a

3-Mose anakwera pa phiri kuti akawonane ndi Mulungu. Ndipo AMBUYE anamuyitana iye kuchokera mphirilo ndikumuwuza kuti, “Uliwuze banja la Yakobo, ndipo ulankhule ndi a Isirayeli onse kuti:
4-“Iwowo anaziwona zinthu zimene ndinachita kwa a Eguputo, ndinakunyamulani inu pa mapiko a nkhwazi, ndikukufikitsani kwa Ine mwini.
5-Tsopano ngati muwamvera mawu anga, ndikusunga chipangano changa, mukhala anthu anga pakati pa anthu a mitundu yonse, ngakhale kuti dziko lonse la pansi lili langa, kwa Ine mudzakhala ufumu wa anthu a msembe ndipo oyera.”

-Kodi Mulungu anamuwuza chiyani Mose pamwamba pa phiri paja?
-Mulungu amkafuna kupereka chipangano kwa a Isirayeli.

-Kodi chipangano chimene Mulungu anapereka kwa a Isirayeli chinali chotani?
-Mulungu anati kuti ngati a Isirayeli akuŵamvera malamulo a Mulunguyo, Iye adzaŵadalitsa iwowo.

-Mose anatsika mphiri muja kuti akaŵawuze zimene Mulungu analankhula.

-Kodi a Isirayeli anamuwuza chiyani Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 19:7-8

7-Chomcho Mose atafika anaŵayitana akuluakulu a a Isirayeli, ndipo anaŵawuza mawu onse amene Mulungu anamulamula kuti aŵawuze.
8-Ndipo anthu onse anayankha pamozi kuti, "Tizichita zonse zimeme AMBUYE anena." Pambuyo pake Mose anapita kukaŵawuza AMBUYE zimene anthu aja ananena.

-A Isirayeli anamuwuza Mulungu kuti adzaŵamvera malamulo onse a Mulungu.

-Kodi a Isirayeli ankaŵakumbukira masiku onse amene samkamumvera Mulungungu aja?
-Iyayi.

-A Isirayeli anayiŵala kuti iwowo sankamukhulupilira Mulungu kuti Iye mpaka aŵapulumutse iwowo pa Njanja Yofifira ija pa nthaŵi imene Farawo ndi asilikali ake ankaŵathamangitsa.



se akundiwona."

-Mulungu anamuwuza Mose kuti Iye adzatsika pa phiri la Sinayi, ndipo a Isirayeli akonzekere.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anakonza zotsika pa phiri la Sinayi?

-Mulungu amkafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuti Iye ndi oyera.
-Mulungu amkafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuti Iye amadana ndi tchimo lina lililonse.
-Mulungu amkafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuti Iye amapereka chilango pa tchimo lina lililonse ndi imfa.

-Mulungu anamuwuzanso Mose kuti alembe malire mphepete mwa phiri la Sinayi.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 19:12-13

12-AMBUYE anati, "Anthuwo akuŵalembere malire kuzungulira phirilo, ndipo ukaŵawuze kuti, "Muwonetsetse kuti musalikwere phirilo kapena kuŵakhuza malire ake, aliyense amene alikhudze phirilo, ayenera kuphedwa.
13-Aliyense asamukhudze munthuyo, koma anthu amugende ndi miyala kapena amulase ndi mipaliro. Kaya idzakhala nyama, mudzayiphe, ngakhalenso munthu, mudzamuphe. Koma mukadzamva kuyimba kwa lipenga, anthu mudzabwere ku phiri."

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anafuna kuti Mose alembe malire mphepete mwa phiri la Sinayi?

ndiye kuti Satana aŵawononga.

-Mulungu yekha ndi amene angatipulumutse ife ku mphamvu ya tchimo.
-Mulungu yekha ndi amene angatipulumutse ife ku mphamvu ya imfa.
-Mulungu yekha ndi amene angatipulumutse ife ku mphamvu ya Satana.

-Apa pali chipangano chimene Mulungu anagwirizana ndi a Isirayeli:

-Ngati a Isirayeli akuŵamvera malamulo onse a Mulungu, ndiye kuti Mulungu aŵadalitsa.

-Ngati a Isirayeli sakuŵamvera malamulo onse a Mulungu, ndiye kuti Mulungu aŵapatsa chilango.

-Kodi Mulungu anati chiyani, Mose atamuwuza kuti a Isirayeli agwirizana ndi zakuti aŵamvera malamulo ake onse?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 19:9a ndi 10-11

9-Ndipo AMBUYE anamuwuza Mose kuti, “Ndibwera kwa iwe mu thambo lochindikala, kuti anthu adzikandimva pamene ndidzikalankhula ndi iwe, kutinso akakhulupilire kwa zaka zonse.”
10-AMBUYE anamuwuza Mose kuti, “Upite kwa anthuwo ndipo ukaŵawuze kuti asakakhale pamodzi ndi azikazi awo lero ndi maŵa. Akachape zovala zawo
11-ndipo akhale okonzeka pa tsiku la nkucha. Ine AMBUYE ndidzatsika pa phiri la Sinayi anthu on-



-A Isirayeli anayiŵala kuti iwowo sankamukhulupilira Mulungu kuti Iye mpaka aŵapatse zakudya ndi madzi mchipululu muja.

-Kodi a Isirayeli ankaganiza zakuti adziŵamvera malamulo onse a Mulungu?
-Inde.

-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli ankaganiza zakuti aŵatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu?
-Chifukwa chakuti iwowo anali adzikonda ndipo adzikweza.

-Kodi a Isirayeli anakatha kuŵamvera malamulo a Mulungu onse aja?
-Iyayi.

-Kodi chifukwa chiyani a Isirayeli sanakatha kuŵamvera malamulo a Mulungu onse aja?
-Chifukwa chakuti anabadwa ali ana a Adamu ndi Hava.
-Chifukwa chakuti anabadwa ali akapolo a tchimo.
-Chifukwa chakuti anabadwa ali akapolo a Satana.

-Anthu onse anabadwa ali ana a Adamu ndi Hava.
-Anthu onse anabadwa ali akapolo a tchimo.
-Anthu onse anabadwa ali akapolo a Satana.

-Kodi Mulungu ankadziŵa kuti a Isirayeli satha kuŵamvera malamulo onse a Mulunguyo?
-Inde.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anapereka

lonjezo kwa a Isirayeli akudziŵa kuti iwowo sanakatha kuŵamvera malamulo Ake onse?

-Kodi inu mungathe kukhazikitsa chipangano kwa munthu amene mukudziŵa kuti satha kukwaniritsa chipanganocho?
-Iyayi.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anakhazikitsa chipangano ndi a Isirayeli Iye akudziŵa kuti iwowo sakwaniritsa chipanganocho?

-Mulungu anakhazikitsa chipanganocho chifukwa chakuti Iye ankafuna kuŵaphunzitsa chilungamo chofunika kwambiri a Isirayeli.

-Kodi ndi chiyani chemene Mulungu ankafuna kuŵaphunzitsa a Isirayeli?

-Mulungu ankafuna kuŵaphunzitsa a Isirayeli kuti iwowo sangathe kuŵamvera malamulo Ake onse.

-Ngakhale kuti a Isirayeli anakalimbikira kwambiri, sanakathabe kuŵamvera malamulo onse a Mulungu.

-Mulungu ankafuna kuŵaphunzitsa a Isirayeli kuti ngakhale anakalimbikira kwambiri, sanakathabe kuŵamvera malamulo onse a Mulungu chifukwa chakuti iwowo anabadwira mu tchimo.

-Mulungu ankafuna kuŵaphunzitsa a Isirayeli kuti chifukwa chakuti iwowo sanakatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu, Mulungu yekha ndi amene



anakatha kuŵapulumutsa iwowo ku imfa yosatha.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anachimwa, ana awo onse anabadwira mu tchimo.
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anachimwa, ana awo onse anabadwa ndi tchimo m'mitima mwawo.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anamumvera Satana, ana awo onse anakhala ana a tchimo, imfa ndi Satana.

-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava anamumvera Satana, anaawo onse anakhala akapolo a tchimo, imfa ndi Satana.

-Mulungu ankafuna kuŵawonetsa a Isirayeli tchimo lawo.
-Mulungu ankafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuyipa kwawo.

-Mulungu ankafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuti anali akapolo a tchimo.
-Mulungu ankafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuti anali akapolo a kuyipa.
-Mulungu ankafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuti anali akapolo Satana.

-Mulungu ankafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuti ngati iwowo sakulilira kwa Mulungu kuti aŵapulumutse, ndiye kuti tchimo lawo liŵawononga.

-Mulungu ankafuna kuŵawonetsa a Isirayeli kuti ngati iwowo sakulilira kwa Mulungu kuti aŵapulumutse,